**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO**

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

# NYENGO MSABATAYI

## KUYAMBIRA PA 14 MPAKA PA 20 OCTOBER, 2024


## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Tiyembekezere nyengo yamitambo yapatali patali komanso yotentha msabatayi. Koma pakati pa lachiwiri masana pa 15 October 2024 mpaka lachinayi pa 17 October 2024, tiyembekezere nyengo ya mphepo, yamitambo komanso mvula ya mabingu m'madera ena. Izi zili chonchi kamba ka mphepo zozizila komanso zachinyotho zochokera kumwera chakumvuma zomwe zikhale zikukumana ndi mphepo zofunda zochokera kumvuma.

***Mphepo ya Mwera zikuyembekezereka kuomba mwamphanvu pa nyanja ya Malawi ndi nyanja zina kuyambira lachiwiri masana pa 15 October 2024 mpakana lachinayi pa 17 October 2024.***

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

M'madera ambiri kunali nyengo yamitambo komanso yofunda ndipo m'madera ena monga akumpoto kunagwa mvula. Madigiri akatenthedwe anatsika kwambiri m'madera ozungulira Mulanje ndi Phalombe poyerekeza ndimomwe kwakhala kukutenthera m'mwezi wa October m'zaka zambuyomu (Onani mapu munsimu)**.**




**Chithuzichi chikuonetsa kusiyana kwa madigiri akatenthedwe msabata yangothayi poyerekeza ndi momwe madigiri amakhalira m'mwezi umenewu wa October m'zaka za 1991-2020.**

## MALANGIZO M'SABATALI

- **Nyengo ya mphepo pa nyanja:** Asodzi ndi ena ogwiritsa ntchito nyanja akhale osamala.
- ***Nyengo yotentha ndi ya dzuwa****: Tizimwa madzi pafupipafupi komanso tisamakhalitse pa dzuwa.*
- ***Nyengo ya ziphaliwali****: Tikhale malo otetezeka komanso tipewe kukhala pansi pamitengo pomwe mvula ikugwa.*

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 13 October, 2024**